



MASEWERO A ZISUDZO (Drama)



International
Labour
Organization

TIMVERENI

Lekani Kugwiritsa tchito Ana

Kulimbikitsa Ufulu wa Ana Kudzera M'maphunziro,
Zaluso ndi Njira zofalitsira Mauthenga



TIMVERENI

Lekani Kugwiritsa Ntchito Ana

**Kulimbikitsa Ufulu wa Ana Kudzera M'maphunziro,
Zaluso ndi Njira zofalitsira Mauthenga**

Masewero a Zisudzo

Kabukuka ndi kamodzi ka mabuku a maphunziro a TIMVERENI Lekani Kugwiritsa Ntchito Ana. TIMVERENI ndi maphunziro olimbikitsa ufulu wa ana kudzera m'maphunziro, zaluso ndi njira zina zofalitsira mauthenga. Mabukuwa analembedwa mu chaka cha 2011 ngati mbali imodzi ya pulojekiti ya IPEC/ILO ndi chithandizo chochokera ku boma la Italy.

IPEC/ILO ikulimbikitsa kuti mabukuwa angathe kuyikidwa mu zilankhulo zosiyanasiyana komanso kusindikizidwanso kuti ntchito yothetsa nkhanza kwa ana ipite patsogolo. Ngati mwatanthauzira bukuli mu chinenero china kapena kusinthako mbali ina ya mabukuwa, kumbukirani kunena komwe mwatenga uthengawo ndiponso mutumizireko a ILO/IPEC mabukuwa kapena mbali yomwe mwasintha.

TIMVERENI–Lekani Kugwiritsa Ntchito Ana. Kulimbikitsa ufulu wa ana kudzera m'maphunziro, zaluso ndi njira zofalitsira mauthenga, Ntchito Yolimbana ndi Mchitidwe Ogwiritsa Ntchito Ana pa dziko lonse, International Programme on the Elimination of Child Labour (IPEC), International Labour Office (ILO), Geneva, 2011.

ISBN N. 92-2-113 240-4

Mungathe kudziwa zambiri za TIMVERENI kuchokera ku:
International Programme on the Elimination of Child Labour (IPEC)
International Labour Office (ILO)

4, Route des Morillons, CH-1211 Geneva 22, Switzerland
Telephone: +41 22 799 7747
Fax: +41 22 799 81 81
Email: childlabour@ilo.org
Web site: www.ilo.org/scream

Cholinga: Kukonzekera ndi kuwonetsa sewero la zisudzo pa nkhani ya kulemba ntchito ana ang'ono.



Phindu lake: Kuthandiza kuti achinyamata akhale omasuka polankhula ndi kunena za kukhosi. Masewero azisudzo amathandizanso kuti anthu ambiri azindindikire ndi kutenga mbali pa nkhani za chitukuko.

Nthawi

Zigawo zisanu ndi chimodzi za kuphunzitsa kuphatikizapo nthawi yokonzekera komanso yowonetsa sewero.

Chidziwitso



Phunziro ili likuthandizira maphunziro ena monga la Chithunzithunzi (Image), Masewero Oyerekeza Zochitika Zenizeni (Role Play) komanso phunziro la Kulemba za Nsangulutso. Likulimbikitsa zomwemunaphunzira kale monga kupereka chithunzithunzi cha Khalidwe lolemba ntchito ana ang'ono, kudziwa luso la kulemba, komanso kukonzekera ndi kuwonetsa sewero. Choncho sibwino kuyamba phunziro limeli musanaphunzireza mu mabuku amene atchulidwawa.

Nthawi zina ana, makamaka achinyamata otha msinkhu kumene, amakhala amanyazi pakati pa anzawo a msinkhu wawo ndipo sakhala omasuka kunena zomwe akukumana nazo m'moyo wawo, makamaka ngati sanachiteko masewero a zisudzo. Choncho onenetsetsani kuti iwo akuthandizidwa kuti akhale omasuka. Gwiritsani ntchito njira ya sewero yongoyerekeza zomwe zingachitike pa nkhani ya Khalidwe lolemba ntchito ana ang'ono komanso luso lopeka nkhani kuti anawa ayambe kumasuka ndi kukhala ndi chidwi chonena zakukhosi kwao pa zomwe akukumana nazo m'moyo wao. Athandizeni kuzindikira mosawakakamiza.

Chilimbikitso



Kafukufuku amasonyeza kuti anthu amuphunzira komanso kusinthika kudzera mu sewero potengera ndi momwe aliwonera sewero. Potsata njira zomwe zili pansizi, achinyamata angathe kuphunzira zinthu zatsopano komanso kusinthika m'moyo wawo.

- Kukhala ndichidwi munkhanizopeka;
- Kudziganizira ngati nawonso alowa awo ndi kukhala nawo mu nkhanizopeka ngati kuti kuchitika;
- "Kudziwa ndi kuchita nawo" zonse monga kusankha zochita, komanso zochitika zonse zomwe anthu a musewero akuchita kuphatikizapo zotsatira zake;
- Kulumikiza zonsezi ndi zomwe zikuchitika pa moyo wao.

Cholinga cha zisudzo ndi kukamba nkhani kudzera mu sewero. Nkhani imakambidwa kudzera mu zomwe akuchita anthu a mu sewero pa mitu ya nkhani zosiyanasiyana. Mu phunziroli, mutu wa nkhani ndi mchitidwe ogwiritsa ntchito ana.

Mu phunziro la Masewero Oyerekeza Zochitika Zenizeni (Role-Play), gulu linayamba kumvetsetsa za mavuto omwe ana a pantchito amakumana nawo. Komanso mu phunziro la Kulemba mwa Luso munaphunzira za kalembedwe ka nkhani. Tsopano ndi nthawi yosonyeza zomwe tingathe kuchita ndi luso lomwe munaphunzira polemba panokha sewero lanu, yofotokoza nkhani yanu, maloto anu komanso maganizo anu.

Phunziroli likulimbikitsa kumasuka ponena zakukhosi komanso kuganizira mozama za mavuto a mchitidwe ogwiritsa ntchito ana. Kudzera mu zochitika mu sewero, achinyamata akhala ndi mwayi zokamba zakukhosi kwao zomwe zakhala zikusanthulidwa mu maphunzirowa. Cholinga cha sewero la zisudzo ndi kuyerekeza zomwe zingachitike mu dziko pa nkhani zosiyanasiyana. Kudzera mu sewero, gulu lidzakhala ndi mwayi oyerekeza mu zochita, nzeru ndi maganizo awo zinthu zonse zomwe zingachitike mu nkhani yongopeka. Zochitika mu sewero zimatsata zomwe anthu omwe ali mu seweroli akuchita, kuganiza komanso zomwe ena akuwachitira. Sewero limakhala ndi anthu opezeka mu sewero, zochitika, komanso thawi ndi malo.

Sewero ndi njira yapadera yophunzirira zinthu zozama. Ndi zodziwika kale kuti nkhani zakuphwanya ufulu wachibadwidwe monga kulemba ntchito ana an'gono zikuchitika m'madera ambiri. Anthu ena angathe kuganiza kuti kwao kulibe vutoli ndikukhala osalabadira za nkhaniyi. Anthu ayenera kusintha kaganizidwe, zochita komanso khalidwe osatengera komwe akukhala kapena kutukuka kwa dera lawo. Masewero a zisudzo komanso za luso zina ndi zomwe zingathe kuthandiza kuti anthu asinthe.

Cholinga cha phunziroli ndi kuthandiza achinyamata kuti adziwe kufunika kwa kutianthu asinthe komanso kuzindikira kuti anthu makhala okonzeka kusintha. Mu phunziroli anthu akuzindikira bwino za mavuto a ana chifukwa nkhaniyi yaikidwa mu sewero lolembedwanso ndi ana. Kudzera mu sewero anawa akukamba nkhani yawo kwa ena motero uthenga ungathe kufikira anthu ambiri kuti achitepo kanthu.

Zofunikira

Zofunika pa phunziroli ndi zochepa. Musavutike ndi kupanga sewero lomwe lidzafune zinthu zambiri monga magetsi, zipangizo zoyimbira monga wailesi kapena kukhometsa zipangizo zambiri za pa nsanja (stage). Sewero lanu ndi la nkhani yokhudza ana apantchito omwe ndi osauka. Choncho sewero lanu ndilosafunika zinthu zovuta kupeza.



Gwiritsani ntchito zinthu zomwe mungakwanitse kupeza. Palibe kanthu ngati kudera kwanu kulibe malo opangirako masewero monga holo(hall). Mungathe kukonzekera masewero anu ngakhale mkalasi ya pa sukulu ya m'dera lanu, kapenso panja ngati nyengo ili bwino. Zofunika mu sewero lanu zimatsatira momwe mwalemba sewero. Zochitika mu phunziroli ndi za gulu lonse pamodzi choncho pezani malo okwanira kukhala gulu lonse.



Chidziwitso

Phunziroli ndi lotopetsa kwa inu komanso gulu lonse. Choncho konzani nthawi yopumira yokwanira pa nthawi yolembe ngakhale kukonzekera sewero. Achinyamata amafunika nthawi yopuma yokwanira komanso yosewera kuti akwaniritse kuganiza moyenera komanso kugwira bwino ntchito. Apatseni nthawi yokwanira yothandiza kuti matupi awo amasuke komanso akhale ndi mpata wakudya kuti akhale ndi mphamvu pa nthawi yokonzekera sewero. Onetsetsani kuti apumula mokwanira nthawi yowonetsa sewero isanafike. Aliyense ayang'anire bwino za umoyo wake pa nthawi ya zochitika za mu phunziroli.

Kukonzekera



Ngati ndi koyenera ndipo ngati mungakwanitse, werengani ndikuchita kafukufuku okwanira pa mutu ogwiritsa ntchito masewero a zisudzo ngati njira yophunzitsira. Kupeza mabuku a masewero ndi kosavuta ngati masewero a zisudzo ali pa m'ndandanda wa maphunziro a sukulu za m'dera lanu. Mungathe kupezanso mabukuwa ku nyumba zowerengerako komanso pa makina a komputa (internet). Komanso mungathe kupempha anthu omwe amadziwa bwino za masewero a zisudzo kuti akuthandizeni pa phunziroli.

Ngati simukudziwa bwino za masewero a zisudzo, ***Chithandizo chapadera*** onetsetsanikuti mwapeza munthu wodziwa bwino zamasewero kuti akuthandizeni kuphunzitsa phunziroli. Ngakhale ndinuozindikira pang'ono, pezanibe munthu amene ndiodziwa bwino za masewero azisudzo.

Kufunika kwa mlangizi wa zisudzo kudzatengera ndi zolinga za gulu lanu pokonza sewero. Mwa chitsanzo, ngati cholinga cha sewero lanu ndi kupititsa patsogolo ntchito anu ndiye kuti padzafunika munthu wodziwa bwino za ulemba komanso masewero a zisudzo. Akatswiri ena a masewero angathe kukhalanso dziwa bwino kulemba komanso ena olemba angathe kukhala odziwa za masewero. Mungathe kuwapemphanso omwe anakuthandizani mu phunziro la Kulemba za Nsangulutso komanso Masewero Oyerekeza Zochitika Zenizeni (Role-play) ngati angakhalenso ndi mpata.

Ngakhale kuti aliyense amafuna malipiro akagwira ntchito, zindikirani kuti sinthawi zonse pamene mudzafunike kuwalipira akatswiri a masewero a zisudzowa. Ngati muli pa ubale ndi akatswiriwa, kapena kuti ndi okhudzidwa ndi zomwe mukupanga, iwo angathe kukuthandizani ndi malipiro ochepa kapena popanda kuyembekezera malipiro aliwonse. Musaope kuwafotokozera za zolinga zanu kuti amvetse kufunika kwa chithandizo chawo pa nkhanayi. Ndi bwino kulephera koma mutayesa!



Gawo loyamba la zochita: Kulemba Sewero

Maphunziro atatu



Pali maganizo awiri (osiyana) okhudza nkhani yolembe sewero. Akatswiri ena amanena kuti sewero lolembedwa limalepheretsa ochita sewero kulankhula momasuka. Ena amanena kuti sewero lolembedwa limachotsa mantha komanso manyazi kwa ana makamaka omwe sanachiteko sewero. Ife tinaona kuti ana ambiri omwe tinapanga nawo masewero pa nthawi yoyeserera phunziroli anali omasuka chifukwa anathandizidwa ndi sewero lolembedwa. Anthu ali ndi ufulu otsatira sewero lonse lolembedwa koma ngati nkoyenera zinthu zina zingathe kusinthidwa pa nthawi yokonzekera sewero.

Ndi zinthu zambiri zomwe zingabweretse maganizo opezeka mu sewero. Sewero lingathe kukhala nkhani yomwe inachitikira ena kapena m'modzi wa gulu lanu. Mwina ena amagwira ntchito kapena anagwirako ntchito adakali ana ang'ono. Komanso ndi zotheka kutenga nkhani zomwe munalembako mu phunziro la Kulemba Mwaluso kapena mu maphunziro ena ndi kuziyika mu sewero. Zina zingathe kuchokera ku zitsanzo (zochititsa chidwi) zomwe alangizi ena anaperekako zokhudza mavuto omwe ana apantchito anakumana nazo ku madera kwina.

Cholinga cha gawoili ndi kukonza nkhani ya sewero potsata mabokosi anayi omwe munaphunzira mu phunziro la Kulemba mwa luso. Bokosi loyamba ndi chiyambi cha nkhani, Bokosi lachiwiri ndi lachitatu ndiye tsinde la nkhani pamene Bokosi lachinayi ndi mathero a nkhani. Choncho nkhani yonse ndi kumasulidwa kwa zochitika mu Bokosi loyamba mpaka lachinayi.

Kukonza nkhani ya sewero

kambiranani maganizo agulu pa mfundo zosiyanasiyana monga zalembedwa pansipa polingalira zomwe munaphunzira, kuona ndi kuchita mu maphunziro a m'mbuyo.

- **Uthenga:** Kodi ndi uthenga wanji omwe gulu likufuna kufalitsa kwa anthu? Kodi mukufuna kupeza chithandizo kuchokera kwa iwo? Kodi mukufuna kuwadzidzimutsa? Kodi mukufuna kudzutsa malingaliro awo ozama?
- **Kochitikira nkhani:** Kumene nkhani ikuchitikira komanso mtundu wa malo a ntchito. Kodi kuli ana okakamizidwa kugwira ntchito? Kodi ndi ana ongoyendayenda? Kodi amakhala kunyumba kwawo? Kodi amapita kusukulu ndi ku ntchito komwe?
- **Anthu a mu sewero:** ana apantchito, olemba anthu ntchito, makolo, alendo, chibale, adani ndi ena otero. Kodi mudzagwiritsa ntchito maina ati?
- **Gawo loyamba la sewero:** Kodi lidzayamba bwanji?
- **Gawo lomaliza la sewero:** Kodi nkhani ya sewero idzatha bwanji? Kodi idzatha ndi chiyembekezo, kuti zinthu zikhala bwino (zingakhale bwino sewero litatha motero)?
- **Kutenga mbali:** Kodi gulu lonse lidzatenga nawo mbali mu nkhani ya sewero? Kodi ena



Izi ndi zina mwa zinthu zomwe mungakambirane mu gulu lanu. Monga mlangizi muyenera kuzindikira kufunika kolimbikitsa uthenga wa chiyembekezo chabwino mu zochitika zonse za **IPEC**. Zindikirani kuti pochita maphunzirowa mwagwira ntchito yaikulu yothandiza kuthetsa khalidwe lolemba ntchito ana ang'ono. Masewero a zisudzo amathandiza kuti mauthenga wofunika afike kwa anthu ambiri.

Limbikitsani anthu a m'gulu lanu kuti akhale tcheru ndi kulankhula momasuka pa nthawi ya phunziroli. Azindikire kuti ali ndi mwayi tsopano wokamba zakukhosi pa nkhani yowakhudza pogwiritsa ntchito sewero lokonza okha.

Lembani maganizo onse pa bolodi kapena pa pepala. Aliyense akanena maganizo ake, tsekani zokambirana. Perekani nthawi yopumulira pamene inu mukuyika zonse zomwe zakambidwa mu ndondomeko yomveka bwino.

Tsopano athandizeni kukonza nkhani ya sewero potsata njira yamaBokosi anayi aja. Onenetsani kuti aliyense akutengapo mbali ndiponso kuti palibeamene akutchingira pa zochitikazi.

Kulemba nkhani ya mu sewero



Mukamaliza kulemba ndondomeko ya nkhani muyenera kuyamba kulemba nkhani yonse mwatsatanetsatane, kulumikiza chiyambi mpaka mathero a nkhani. Imeneyi ndi nthawiyokambirana zonse zopezeka mu sewero monga zolankhula anthu amusewero, zochita zawo ndi zonse zofunika kuti sewero liyende bwino. Ngati gulu lonse ndilokonzeka kugwira ntchitoyi, muyenera kuyendetsa zokambiranazi mwa luso lapadera kuti pasakhale chisokonezo. Ndizosangalatsa ngati gulu lonse awonetsa chidwi chotenga mbali polemba nkhaninyi.

Funsani munthu m'modzi kapena awiri kuti adzilemba maganizo onse. Ndi zotheka kugwana mu magulu a anthu awiri, atatu kapena asanu ngati gulu ndi lalikulu kwambiri, monga la anthu khumi. Apatseni magulu amenewa ntchito zosiyanasiyana kuti apange. Mwachitsanzo, gulu limodzi lingathe kunena za anthu opezeka mu nkhani ya sewero (characters), ena angathe kukambirana zochitika mu gawo loyamba la sewero ndipo gulu lina likambirane zochitika ngati tsinde la sewero. Ndi zothekanso kuti gulu lililonse lilemba nkhani yonse pawokha. Zikatero ndiye kuti mukhala ndi nkhani zingapo. Mukatero mungathe kulumikiza nkhanizi ndi kupanga nkhani imodzi yokomera gulu lonse. Onetsetsani kuti aliyense akuzindikira kuti nkhani yomwe yalembedwa yachokera m'maganizo awo. Izi zidzalimbikitsa aliyense kukhala odzidalira komanso kukhala ndi chidwi pa zochitikazi.

Kumapeto a zonse muyenera kulumikiza maganizo onse ndi kuonetsetsa kuti sewero lomwe lalembedwa likumveka bwino. Nthawi zina gulu lingathe kukhala ndi maganizo akuthwa kapena ozama kwambiri. Mwina maganizo ena angakhale ovuta kuwakwaniritsa. Musade nkhwana ndi zimenezi. Gulu lingathe kukwaniritsa kupanga *sewero* li chifukwa zomwe zalembedwa zachokera mu nzeru zawo, komanso chifukwa mwaonetsa chidwi kuti muwathandiza.



Cholinga chenicheni cha phunziroli ndi kuti achinyamatawa adziwe za mchitidwe ogwiritsa ntchito ana osati kulemba sewero lotchuka pa dziko lonse (ngakhale kuti zingathe kutheka). Chofunikira kwambiri ndi kuzindikira kuti mungathe kufalitsa mauthenga kwa anthu ambiri chifukwa sewero lingathe kuwonetsedwa malo ambiri.

Kumalizitsa kulemba sewero

Choncho, chigawo ichi ndi nthawi yolumikiza nkhani yonse komanso anthu onse a mu sewero. Ndi nthawi yowona zomwe a musewero akunena komanso kuchita ndi kusankha ngati mu sewero mukufunika nyimbo kapena gule.

Iyi ndi nthawi yowunika uthenga omwe gulu lasankha kuti lifalitse. Gulu lisankhe chilankhulo chomwe iwo amagwiritsa ntchito ndipo amatha kumvana bwino ndi anzawo. Ngati mu nkhani ya musewero muli achinyamata, achinyamatawo ayenera kulankhula momwe iwo amalankhulira. Atsogolereni kuti alankhule monga momwe amalankhulira nthawi zonse ndi kuwonetsetsa kuti akuwonetsadi zomwe zili mu mtima mwao. Ngati gawo lina la sewero silikulumikizana bwino ndi gawo lina, athandizeni kuti zochitika zonse za musewero zimveke bwino.



Mu gawo limeneli mungathe kupemphanso katswiri olemba kapena wa masewero kuti akuthandizeni mu ndime yomaliza kulemba sewero. Kumbukirani kuti cholinga cha phunziroli sikulemba sewero kokha, koma kuti gulu likhale ndi mpata otenga nawo mbali mu zochita-chitazi. Choncho musawasiyire ntchito yonse anthu amene abwera kudzakuthandizani.



Chidziwitso

Kumbukirani kuti simuyenera kuchulutsa zochita mu phunziroli. Monga tanena kale, chidwi cha achinyamata kapena ana chingathe kuchepa ngati zochita zachuluka. Onetsetsani kuti phunziro lisapitirire mphindi makumi awiri kapena atatu. Mudziganizirensomphamvu zanu ngati mungakwaniritse kutsogolera zonse zokhudza kukonzekera sewero makamaka ngati ambiri akungoyamba kumene kudziwa zamasewero azisudzo. Kukonzekera sewero kumafunika kubwerezabwereza zochita choncho ena angathe kutopa. Ndi kofunika kuti gulu lidziwiretu kuti kunzekera sewero kumafunika zinthu zambiri komanso kudekhandi kupirira.

Ndi kotheka kuti gulu lilembe masewero a mitundu ingapo panthawiyi. Zonse zingatheke motsatira kukula kwa gulu uthenga omwe mukufalitsa, malo komanso chikhalidwe cha m'dera lanu. Mwachitsanzo, gulu lingathe kulemba:

- Sewero lofunika kuti gulu lonse titenge mbali mu nkhani ya musewero;
- Sewero lofunika kugawana zochita, ena opanga sewero pamene anzawo akuthandizira pa ntchito zina monga kuyimba ndi kukonza pa bwalo la sewero;
- Sewero lachinunu (lopanda mawu);
- Timasewero ting'onoting'ono, tomwe angapange ndi anthu amodzimodzi kapena osiyana;
- Nyimbo yoyimbidwa ndi gulu lonse kapena anthu ochepa;
- Sewero lopangidwa ndi mwini nkhani (**character**) m'modzi kapena awiri.

Mitundu ya masewero ilipo yambiri. Chofunika kwambiri ndi kuwonetsetsa kuti aliyense watenga nawo gawo pokonza sewero ndi kuzindikira kuti ali ndi udindo pa zochitika zonse.

Monga masewero azisudzo, anthu a mitundu yonse amayimba nyimbo ndipo zimalimbikitsa chikhalidwe chawo. Mungathe kugwiritsanso ntchito nyimbo mu zochitika za TIMVERENI. Choncho mungathe kuwonjezera nyimbo mumasewero anu. Mungathe kutero ngati gulu likufuna, kapena ngati mu gulu muli anthu aluso loyimba komanso ngati zida zoyimbira zilipo.

Mukafika pamenepa, mungathe kuyamba kukonzekera sewero. Ndondomeko ya nthawi yokonzekera sewero iyenera kugwirizana ndi zomwe mukufuna kukwaniritsa:

- Kodi sewero lidzawonetsedwa kwa eni ake a gulu okha?
- Kodi mudzaonetsa seweroli ku sukulu yanu ndi masukulu ena?
- Kodi mudzaonetsa seweroli m'mudzi wanu ndi midzi ina?
- Kodi seweroli mudzaliwonetsera kuti? Mkalasi? Mu malo ochitira masewero **(hall)?** Kapena panja?
- Kodi seweroli likakhala kalambula bwalo wa sewero lina?
- Kodi sewero lanu likakhala nawo pa m'ndandanda wa masewero ena monga mpikisano wa masewero?
- Kodi lidzaonetsedwa kamodzi kapena kangapo kwa anthu osiyanasiyana?
- Kodi sewero lanu lidzagwiritsidwa ntchito yofalitsa mauthenga ngati gawo limodzi la zochitika zanu?
- Kodi mudzayitana atolankhani pa tsiku lowonetsa sewero lanu?

Zonse zidzatsata zomwe gulu likufuna komanso zipangizo zomwe zapezeka monga malo owonetsera sewero komanso kudzipereka ndi chithandizo chochokera kwa anthu ena. Lolani gulu lisankhe zomwe likufuna ndi kukwaniritsa maloto onse. Chofunika kwambiri ndi kuzindikira kuti iwo aphunzira luso latsopano lomwe angathe kugwiritsa ntchito pa nthawi yomwe akukula komanso m'tsogolo. Zonse zomwe aphunzira zidzasintha maganizo awo pa ntchito yolimbana ndi mchitidwe olemba ntchito ana ang'ono.

Kugawana malo mu sewero

Aliyense akhale ndi mpata osankha omwe akhale mu sewero. Ntchito ya mlangizi ndi kungowongolera zochitika. Pa nthawiyi, ngati munachita kale phunziro la Masewero Oyerekeza Zochitika Zenizeni **(Role-play)** mwayenera kudziwa bwino luso la aliyense wa m'gulu lanu.

Chidziwitso

Lolani kuti gulu lisankhe amene akhale mu sewero. Sibwino kumangosankha anthu amodzimodzi kuti akhale 'munthu woyipa' mu sewero. Njira ina yopewera vutoli ndi kusankha anthu odzakhala mu sewero pa nthawi yomwe mukulemba sewero. Nthawi zina mungathenso kusankha kugwiritsa ntchito mayina enieni a anthu omwe adzapezeke mu sewero ngati eni mainawo avomereza. Zimenezi zingathenso kuthandiza kuti musavutike kuloweza mawu a mu sewero.



Gawo lachiwiri la zochita: Sewero

Maphunziro awiri kuphatikizapo nthawi yokonzekera sewero komanso kuwonetsa sewero

Ndi zotheka kuti ambiri mwa anthu a m'gulu lanu anapangapo kale sewero ndipo akudziwa bwino zoyenera kuchita. Koma ngakhale zili choncho ndi koyenera kukhala ndi nthawi yokonzekera yokwanira kuti aliyense akhale omasuka komanso opanda manyazi. Ndi chifukwa chake ndi koyenera kupanga phunziro la Masewero Oyerekeza Zochitika Zenizeni (**Role Play**) musanapange la masewera a zisudzoli. Mukatero mwana aliyense adzakhala atazolowera kukhala omasuka pa zochitika za mu sewero.

Zochitachita pokonzekera sewero

Pali zinthu zingapo zomwe mungachite kuti matupi komanso maganizo akhale omasuka. Mlangizi wa masewero angathe kukuthandizani ndi njira zina zotenthetsera thupi pa nthawi yomwe mukuyamba kukonzekera sewero.

Mungathe kupeza zitsanzo zina za njira zotenthetsera thupi mu Gawo loyambala la Zowonjezera (**Annex 1**) ya phunziro la Masewero Oyerekeza Zochitika Zenizeni (**'Role-Play'**). Mungathenso kupeza zitsanzozina mu mabuku a masewero a zisudzo kuchokera ku nyumba zowerengerako mabuku komanso kwa ogulitsa mabuku. Onetsetsani kuti gulu lachita zotenthetse thupi kosachepera kamodzi poyamba zochitachita zokonzekera sewero.

Kukonzekera sewero ndi achinyamata ndi ntchito yayikulu komanso yosangalatsa. Choncho njira yomwe mungatsate pokonzekera sewero idzatengera ndi zolinga zomwe mukufuna kukwaniritsa. Komanso kutalika kwa nthawi yofunika pa zochitachitazi idatengera ndi zolinga za sewero lanu. Mwa chitsanzo, mudzafuna nthawi yayitali yokonzekera ngati mukuchita nawo mpikisano wa masewero azisudzo kapena kuwonetsa sewero lanu kwa anthu ambiri.

Kukonzekera

Zina zofunika kuziganizira pokonzekera sewero ndi zipangizo komanso malo opangira. Kupeza malo opangira zokonzekera sikuvuta ngati mukupangira ku sukulu kwanu chifukwa sukulu zambiri zili ndi malo opangira masewero. Koma ngati muli kumudzi, mungathe kupeza malo monga bwalo la kwa amfumu, pa tchalitchi ngakhale pansi pa mtengo. Malo ena owonetsera sewero angathe kukhala pa bwalo la msika ngakhale mphepete mwa msewu.

Khalani odekha pa nthawiyi chifukwa kukonzekera sewero kumatenga nthawi yayitali komanso kubwerezabwereza zochita kungathe kuwatopetsa achinyamata. Perekani nthawi yokwanira ku magawo onse a sewero ndipo onetsetsani kuti muli ndi chidwi ndi aliyense ngakhale panthawi yomwe zochitika zikukhudza anthu ochepa.

Perekani nthawi yokwanira yopumulira. Aloleni anawa kuti abweretse zoseweretsa pa nthawi yopumulira monga mpira ngakhale bawo. Ngati ena ali ndi ntchito ya kusukulu (**homework**), aloleni kuti apange pa nthawi yopumulira.

Nthawi zina pa bwalo lopangira sewero pamafunika zinthu monga mipando ndi zipangizo zina. Sankhani ena a mu gulu kuti athandize pa zofunikirazo monga kunyamula mipando, kuyimba nyimbo kapena ng'oma. Zimenezinso zimafunika kukonzekera bwino monga kupatsana ma udindo moyenera kuti sewero lidzachitike mwadongosolo. Kukonzekera mokwanira kudzanthandiza kuchotsa nkhwana kapena mantha ndi ntchito yokonzekera ndi kuwonetsa sewero.

Fotokozerani gulu zonse zofunika kuchita pokonzekera sewero. Makamaka kwa gulu lomwe silinapangeko sewero, ndi kofunika kufotokozerana bwinobwino ndondomeko yonse yopangira sewero monga zomwe ayenera kulankhula kapena kuchita komanso nthawi yomwe ayenera kulankhula kapena kuchita zinthu. Mitundu ina ya masewero, monga sewero logwiritsa ntchito zigoba zovala kumaso, imafunikanso kufotokozerana mosamala. Aloleni anawa kuti afunse mafunso ndipo mvetserani ndi kuyankha mafunso onse ndi chidwi.

Njira ina imene imathandiza ochita sewero atsopano ndi kuwonetsetsa kuti sewero lalembedwa ndi malangizo onse ofunikira kuti ochita sewero adziwe zochita komanso momwe angachitire. Izi ndi monga malangizo owunikira ochita sewero kuti 'alankhule mokalipa', 'atuluke', 'athamange akulira', 'apite ku manzere kapena kumanja akamaliza kulankhula' ndi zina zomwe zingafunike kuti ochita sewero adziwe.

Pali zinthu zingapo zofunika kuziganizira tsiku lowonetsa sewero likayandikira, tsiku likafika komanso pochita zina zotsatira sewero likawonetsedwa. Zambiri zinafotokozedwa kale mu maphunziro a Kufalitsa Nkhani ngakhale mu phunziro la Kafukufuku, la Mauthenga komanso la Kulumikiza Anthu a m'Madera ndi Zochitika (**Community Integration**).

Sankhani bwino tsiku lowonetsa sewero powonetsetsa kuti anthu ambiri adzakhala ndi mpata obwera kudzaonera. Muyeneranso kusankha bwino anthu omwe mukufuna adzamve uthenga omwe ukupezeka mu sewero lanu. Adziwitseni eni malo za nthawi yomwe mukukumanirana kuti pasakhale chisokonezo ndi zina zomwe zimachitika pa malowo.



Kuwonetsa sewero

Cholinga chowonetsa sewero ndi kuti maganizo anu afike kwa anthu ndikukwaniritsa maloto anu. Kuti izi zitheke muyenera kudziwa bwino zambiri za anthu amene adzawonere sewero lanu. Mukatero mungathe kukonzekera moyenera. Choncho chitani kafukufuku wa zimenezi. Aliyense atenge nawo mbali pa kafukufuku ameneyu. Ngati mudzawonetse sewero lanu kwa anthu ambiri muyenera kuganizira zinthu izi:



- **Matikiti** – Kodisewero lanu lidzakhala lolipiritsa kapena laulere? Kodi mudzagulitsa matikitiwo pa tsiku la sewero kapena tsiku lisanafike? Kodi mudzayika bokosi kapena mbale pakhoma kuti anthu adzaponyemo ndalama kapena chithandizo chilichonse?
- **Kudziwitsa anthu** – Kodi anthu adzadziwa bwanji zakuti kuli chiwonetsero cha sewero? Kodi mudzalemba makalata ndi kumata m'malo osiyanasiyana monga pa mitengo, pakhoma, ma bus kapena kuwatumizira anthu oyitanidwa?
- **Ndondomeko ya zochitika** – Kodi mudzakhala ndi ndondomeko ya zochitika za patsikuli yolembedweratu (**programme**). Kodi mudzapempha makampani kuti awulutse za malonda awo pa zochitikazi kuti mupezeko ndalama? Kukhala ndi ndondomeko yolembedwa bwino kumathandiza kuti muoneke a dongosolo komanso mungathe kulembamo uthenga othokoza amene akupatsani chithandizo.

Aliyense atenge nawo mbali pa zimenezi. Musawononge ndalama pa zinthu zosafunika. Gwiritsani ntchito zinthu zomwe zilipo kapena zosavuta kupeza ndipo zindikirani kuti chofunika kwambiri ndi kuti sewero lanu lidzaonetsedwe.

Mungathe kuganiziranso zojambula sewero lanu mu kanema. Izi zingathandize mu njira zingapo monga:

- Kutimukonze zomwe munalakwitsa, ngati mukupitiriza kuwonetsa sewero lanu ku malo ena.
- Kugwiritsidwa ntchito mu mauthenga okhudza zochitachita zanu ku nyumba zofalitsira mauthenga.
- Ngati chikumbutso kwa gulu komanso makolo/mabanja awo.
- Kuphunzitsira magulu ena.
- Kupititsa patsogolo mauthenga olimbikitsa kuthetsa khalidwe lolemba ntchito ana ang'ono.
- Kutumizidwa ku **IPEC** kuti ikathandize pa ntchito zothetsa khalidwe lolemba ntchito ana ang'ono pa dziko lonse.

Zoyenera kuchita ndi zoyenera kupewa

- Onetsetsani kuti kusiyana kwa khalidwe la anthu mu gulu kusalepheretse zolinga za gulu
- Aliyense atenge nawo mbali
- Onetsetsani kuti aliyense akhale ndi chidwi kuyambira pa chiyambi mpaka kumapeto a zonse. Pelekani mpata okwanira opumulira.
- Lolani nthabwala kapena nsetso pa nthawi yokumana kuti aliyense akhale omasuka. Onetsetsani kuti izi zikhale nthabwala chabe osati kunyozana.
- Kunyozana kapena kudzudzulana mopanda ulemu ndi kosaloledwa chifukwa zingathe kubweretsa kusagwirizana pa gulu komanso anthu ena angathe kuyamba kufooka.
- Athandizeni omwe akulephera kukwaniritsa zomwe akuchita kuti asachititsidwe manyazi ku gulu. Ngati munthu wayiwala zolankhula kapena zochita mu sewero, athandizeni kapena aloleni kuti achoke pa malo a sewero mosawachititsa manyazi.
- Aganizireninso mwapadera onse amene ali ndi zilema kuti akwaniritse zochitika mu sewero mosavuta. Zindikirani kuti sewero lingathe kuwathandiza kuti amasuke kufotokoza maganizo awo pa zonse zowakhudza. Athandizeninso mwapadera omwe anakhalapo pa mavuto obwera chifukwa cha kulembedwa ntchito ali ana ang'ono. Ngati sewero likuwapangitsa kuti akhale ndi mantha kapena chisoni chifukwa chokumbukira za mavuto awo, athandizeni kuti akhale olimba mtima pa nthawiyi. Makolo komanso atsogoleri angathe kuthandizanso pa nkhani ngati imeneyi.
- Ngati ndi kotheka, jambulani zochitika pa kanema. Izi zidzakuthandizani pa nthawi yomwe mukuwunikanso zomwe mwachita m'mbuyo.
- Mukamaliza kuwonetsa sewero, kambiranani kuti aliyense akhale ndi mpata onena maganizo ake a momwe zinthu zinaliri. Aliyense akhale omasuka. Imeneyi ndi nthawi yabwino yothandiza kuti azamitse nzeru zawo pa zinthu zomwe akuwona ndi maso awo.
- Khalani ndi malingaliro apatali komanso alimbikitseni achinyamata kuti akhale ndi maloto ozama pa zomwe akuchita. Sewero lawo lingathe kubweretsa kusinthika kwa dera lawo komanso madera ena oyandikana nawo. Powona zinthu ngati zimenezi, achinyamatawa angakhale okondwa ndi kukhala olimbikitsidwa komanso odzidalira pa zomwe angathe kukwaniritsa kudzera mu sewero.



Kukambirana komaliza

Phunziro limodzi



Zokambirana za momwe zochitika zayendera ziyenera kuchitika mukamaliza kuwonetsa sewero. Sankhani malo abwino opanda zosokoneza. Onetsetsani kuti zokambirana zanu zichitike nthawi yomwe aliyense ali odekha. Choncho musafulumire kuchita zokambiranazi mpaka aliyense atakhazikika.

Onse amene anakuthandizani pokonzekera sewero lanu angathe kukhalanawo pa zokambiranazi, makamaka mlangizi kapena katswiri wa zisudzo yemwe munamupempha kuti akuthandizeni. Msonkhanitsani zonse zomwe munalemba zokhudza momwe ntchito yonse yayendera kuti zikuthandizeni pa zokambiranazi. Zindikirani kuti maphunziro a TIMVERENI anakonzedwa mu ndondomeko yothandiza achinyamata kuti adziwe za kuyipa kwa khalidwe lolemba ntchito ana ang'ono komanso za ntchito yolimbana ndi khalidweli. Choncho kuchita sewero la zisudzo ndi kothandiza kuti anthu amvetsetse za vutoli komanso zomwe zikuchitika pothetsa mavuto amenewa.

Pa njira zonse zophunzirira, masewero a zisudzo ndi njira yothandiza kwambiri kuti achinyamata amvetsetse bwino za khalidwe lolemba ntchito ana ang'ono komanso zomwe iwo angachite kuti athandize ana omwe akhudzidwa ndi vutoli. Phunziroli lidzathandiza achinyamatawa kuti adziwe bwino za ufulu wa ana komanso kuti akhale odzidalira. Pa mathero a phunziro lililonse iwo adzavomereza ndi kuzindikira za udindo wawo pa nkhani imeneyi komanso kudziwa kuti dziko lonse ndi lokhudzidwa ndipo aliyense ali ndi udindo olimbana ndi vutoli. Komanso ayenera kuzindikira kuti masewero azisudzo ndiothandiza kwambiri pa ntchito yofalitsa mauthenga kwa anthu ambiri osiyanasiyana.

Fotokozerani gulu lanu mwatsatanetsane zolinga za ntchito yonse. Alimbikitseni kuti atenge nawo mbali pa ntchito. Tikuyembekeza kuti achinyamata ndi amene angathandize kwambiri pa ntchito yothetsa kulemba ntchito ana ang'ono. Adzazeni ndi chilakolako komanso maloto othandiza. Azindikiritseni kuti chithandizo chawo ndi chifunika kwambiri makamaka chifukwa iwo ndi amene angathe kumvetsa bwino za mavuto a ana anzawo. Phunziroli lingamalizike bwino mutakwaniritsa zimenezi.

Gawo limeneli ndi lothandiza kuti gulu lizindikire kufunika kwa zomwe apanga. Iwo adzakhala ndi chidwi ndi zonse zochitika ngati zotsatira za sewero lawo komanso masewero ena am'tsogolo. Ndi chinthu chosangalatsa kuwonerera sewero lomwe inu mwathandiza kukonza likuchitika ndipo owonerera akuwonetsa chidwi ndi kuthirira ndemanga. Zimenezizidzakulimbikitsani kuti mukhale ndi chidwi chopititsa patsogolo ntchito zothetsa mavuto okhudza kulemba ntchito ana ang'ono.

Kuwunika momwe ntchito yayendera ndi kuchita kalondolondo

Njira yowunikira momwe ntchito yayendera ndi kuwona ngati mwakwaniritsa kukonza sewero komanso kuwunika chidwi cha gulu pogwira ntchito. Yang'ananinso ngati gulu lanu likuonetsa kusinthika pa zinthu monga: kukhala ozindikira, omasuka komanso odzidalira. Muwunikenso luso pa kachitidwe ka zisudzo kwa amene azindikira kuti iyi ndi njira ya mphamvu yobweretsera kusintha Masewero a zisudzo ndi njira yamphamvu yothandizira achinyamata kuti akwaniritse kuzindikira momwe angathandizire pa ntchito yolimbana ndi khalidwe lolembantchito ana ang'ono. Phunziro limeneli ndi lopambananso chifukwa anthu ambiri amamva za uthengawu kwa nthawi yayitali makamaka ngati likulimbitsa anthu kuti achitepo kanthu.



Choncho masewerowa adzapangitsa kuti anthu a m'gulu lanu akhale anthu obweretsa kusintha komanso chitukuko pothandiza ena kuti aphunzire, kumvetsetsa ndi kusintha chikhalidwe chawo. Anthu adzadziwa momwe ana akuvutikira padziko lonse ndi kuona momwe angathandizire kuti vuto limeneli lithe.

Lembani ndi kusunga pabwino zonse zomwe mwakambirana kuti udzazigwiritsenso ntchito mu maphunziro ena a pulojekitiyi.

Ngati mwaona kuti zochitika za mu phunziroli zayenda bwino, pitirizani ndi phunziro la Kutengera Zochitachita Kumudzi momwe sewero likugwiritsidwa ntchito ngati njira yofunika kwambiri polimbikitsa anthu kuti atenge mbali pa zochitika zothetsa khalidwe lolemba ntchito ana ang'ono komanso kuthetsa mavuto omwe ana apantchito amakumana nawo. Kumbukiraninso kuti cholinga cha maphunziro onse mu ntchitoyi ndi kulimbikitsa anthu onse kuti atenge mbali pa ntchito yothetsa vutoli.

Mungathenso kupitiriza ndi zochitachita zofalitsa mauthenga pogwiritsa ntchito masewero. Kapena, mungathe kupitiriza zochitikazo poyamba kuphunzitsa gulu latsopano. Kumbukirani zonse zomwe achinyamata aphunzira kudzera mu phunziroli ndi kuzindikira kuti moyo wao wasinthika.

Zolembe zina

[illegible]

Zolembe zina

[illegible]

Lekani Kugwiritsa ntchito Ana



ILO
International programme on the
Elimination of Child Labour (IPEC)

ILO/ IPEC Malawi Project
Mantino Complex
Behind Bizonowaty filling station
PO BOX 30135
Lilongwe

Tel: (+265)-0- 1 770 388/ 199/155

www.ilo.org/ipecc

ISBN 92-2-113240-4

